Kumvetsa

PAMENE CINTHU CACING'ONO
CIONEKERA/CIONETSA KULI CINTHU CACIKULU

Zizindikiro zoyamba kuonekera za khansa mwa mwana

- Kodi amamva thupi kutentha kawiri-kawiri?
- Kodi wasintha kapenyedwe mwadzidzidzi? (kusaona, kukula kwa diso, kuona mofinya diso, kapena ali ndi kanthu koyera m'diso.)
- Kodi amakhala wolema nthawi zonse kapena wasinthika khungu?
- Kodi sikelo lace licepekera kapena safuna kudya cifukwa alibe dyokodyoko?
- Kodi ali ndi khungu long'ambika kwambiri, kapena akutuluka magazi kapena ali ndi tumathuza tofiira pa khungu lace?
- Kodi amagwidwa ndi matenda yoyambukiridwa nthawi zambiri?
- Mukamuona bwino, kodi ali ndi cotupa pa mutu, pa khosi, pa mimba, pakati pa miyendo, m'mawere kapena mkhwapa?
- Kodi mafupa ace, m'malungo mwace ndi msana wace ukuwawa? Kapena miyendo yace ndi yotupa?

- Kodi amadwala mutu kawiri-kawiri komanso kusanza m'mawa?
- Kodi mutu wace ndi waukulu kwambili?
- Kodi amamva museluselu kapena amasanza ngakhale sanamve museluselu?
- Kodi waphonya cinthu cacikulu mu umoyo wace, kapena wabwerera kumbuyo?
- Kodi khalidwe lace lasintha?
- Kodi wasintha kayendedwe, kumayenda copendeka kapena mosimphina?
- Kodi amayenda mopendeka kapena amagwa kawiri-kawiri?
- Kodi anathyokapo kale fupa mosayambekezeka, mwina cifukwa ca kugwa?

Zikapitiliza conde pitani ku cipatala popeza zizindikiro zoonekera mofulumira zimathandiza kuteteza myoyo....

Cupcakes 4 Kids with Cancer

NPC 2012/103028/08

Conde khalani *Angelo*...

Njira yotsekemera kwambiri ya

KUTETEZA MOYO

www.cupcakesofhope.org

Thandizani "National Cupcake Day"–29/09/2018

Thank you to Localize Africa for the Chichewa translation